# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Danieli

1. Maleredwe a Danieli ndi anzace kwa mfumu ya ku Babulo
2. Nebukadinezara alota, Danieli ammasulira lotolo
3. Anzace a Danieli aponyedwa m'ng'anjo yamoto
4. Loto la Nebukadinezara la mtengo waukuru
5. Madyerero a Belisazara, dzanja lolemba pakhoma
6. Akalonga amchulira Danieli cifukwa kwa Dariyo

Wodala munthu wakupirira poyesedwa; pakuti pamene wabvomerezeka, adzalandira korona wa moyo, amene Ambuye adalonjeza iwo akumkonda Iye – Yakobo 1.12

- Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Maleredwe a Danieli ndi anzace kwa mfumu ya ku Babulo

**Danieli 1**

1 Caka cacitatu ca Yehoyakimu mfumu ya Yuda, Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo adadza ku Yerusalemu, naumangira misasa ya nkhondo.
2 Ndipo Yehova anapereka Yehoyakimu mfumu ya Yuda, m'dzanja lace, pamodzi ndi zipangizo zina za m'nyumba ya Mulungu, namuka nazo iye ku dziko la Sinara, ku nyumba ya mulungu wace, nalonga zipangizozo m'nyumba ya cuma ca mulungu wace.
3 Ndipo mfumu inauza Asipenazi mkuru wa adindo kuti abwere nao ena a ana a Israyeli, a mbeu ya mafumu, ndi ya akalonga;
4 anyamata opanda cirema, a maonekedwe okoma, a luso la nzeru zonse, ocenjera m'kudziwa, a luntha lakuganizira, okhoza kuimirira m'cinyumba ca mfumu; ndi kuti awaphunzitse m'mabuku, ndi manenedwe a Akasidi.
5 Ndipo mfumu inawaikira gawo la cakudya ca mfumu tsiku ndi tsiku, ndi la vinyo wakumwa iye, ndi kuti awalere zaka zitatu, kuti potsiriza pace aimirire pamaso pa mfumu.
6 Mwa awa tsono munali a ana a Yuda, Danieli, Hananiya, Misayeli, ndi Azariya.
7 Ndi mkuru wa adindo anawapatsa maina ena; Danieli anamucha Belitsazara; ndi Hananiya, Sadrake; ndi Misaeli, Mesaki; ndi Azariya, Abedinego.
8 Koma Danieli anatsimikiza mtimti kuti asadzidetse ndi cakudya ca mfumu, kapena ndi vinyo amamwa; cifukwa cace anapempha mkuru wa adindo amlole asadzidetse.
9 Ndipo Mulungu anamkometsera Danieli mtima wa mkuru wa adindo, amcitire cifundo.
10 Nati mkuru wa adindo kwa Danieli. Ine ndiopa mbuyanga mfumu, amene anakuikirani cakudya canu ndi cakumwa canu; pakuti aonerenji nkhope zanu zacisoni zoposa za anyamata olingana ndi inu? momwemo mudzaparamulitsa mutu wanga kwa mfumu.
11 Nati Danieli kwa kapitao, amene mkuru wa adindo adamuikayo ayang'anire Danieli, Hananiya, Misaeli, ndi Azariya,
12 Muyesetu anyamata anu masiku khumi; atipatse zomera m'nthaka tidye, ndi madzi timwe.
13 Pamenepo mupenye maonekedwe athu ndi maonekedwe a anyamata akudya cakudya ca mfumu; ndi monga umo muonera, mucitire anyamata anu.
14 Ndipo anawamvera mau awa, nawayesa masiku khumi.
15 Atatha masiku khumiwo tsono, anaona kuti maonekedwe ao ndi kunenepa kwao anaposa anyamata onse adadyawo zakudya za mfumu.
16 Pamenepo kapitaoyo anacotsa cakudya cao ndi vinyo akadamwa, nawapatsa zomera m'nthaka.
17 Koma anyamata amene anai, Mulungu anawapatsa cidziwitso ndi luntha la m'mabuku ali onse, ndi nzeru; koma Danieli anali nalo luntha la m'masomphenya ndi maloto onse.
18 Atatha masiku inanenawo mfumu kuti alowe nao, mkulu wa adindo analowa nao pamaso pa Nebukadinezara.
19 Ndipo mfumu inalankhula nao, koma mwa iwo onse sanapezeka monga Danieli, Hananiya, Misaeli, ndi Azariya; naimirira iwo pamaso pa mfumu.
20 Ndipo m'mau ali onse anzeru ndi aluntha, amene mfumu inawafunsira, inawapeza akuposa alembi ndi openda onse m'ufumu wace wonse.
21 Nakhala moyo Danieli mpaka caka coyamba ca Koresi.

**Mafunso**

1. Ndi ciani cimene cinacitika kwa Danieli, Hananiya, Misayeli ndi Azariya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mkuru wa adindo anamuca dzina lotani Danieli? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Cifukwa ciani Danieli anatsimikiza mtima kuti asadzidetse ndi cakudya ca mfumu kapena ndi vinyo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mkuru wa adindo anayankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

5. Kodi Danieli anamuuza ciani kapitao? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Danieli ndi anzake anaoneka bwanji pambuyo masiku khumi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Mulungu anapatsa ciani kwa anyamata aja anai? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Mulungu anadalitsa Danieli ndi anzake cifukwa anamvera malamulo a Mulungu. Kodi mumamvera malamulo a Mulungu?
9. Kodi tingaphunzire bwanji kumvera Mulungu?

**Sewero**

Pezani mau onse.

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| d | a | n | i | e | l | i |
| r | n | u | m | u | f | m |
| n | z | e | r | u | o | n |
| c | a | k | u | d | y | a |
| i | k | h | b | b | n | z |
| a | e | u | l | s | i | m |
| n | t | m | b | p | v | y |
| i | w | i | z | d | a | m |

- khumi
- ciani
- vinyo
- danieli
- mfumu
- madzi
- anzake
- cakudya
- nzeru

## 2. Nebukadinezara alota, Danieli ammasulira lotolo

**Danieli 2**

1 Caka caciwiri ca Nebukadinezara mfumu, Nebukadinezarayo analota maloto, ndi mzimu wace unabvutika, ndi tulo tace tidamwazikira.

2 Pamenepo mfumu inauza munthu aitane alembi, ndi openduza, ndi aula, ndi Akasidi, amuululire mfumu maloto ace. Nalowa iwo, naimirira pamaso pa mfumu.

(…)

9 Koma mukapanda kundidziwitsa lotoli, mlandu wanu ndi umodzi; popeza mwapanganiranatu mau onama ndi oipa, kuwanena pamaso panga, mpaka idzasanduka nyengo; cifukwa cace mundifotokozere lotoli, momwemo ndidzadziwa kuti mudzandidziwitsa kumasulira kwace komwe.

10 Akasidi anayankha pamaso pa mfumu, nati, Palibe munthu pa dziko lapansi wokhoza kuulula mlandu wa mfumu; cifukwa cace palibe mfumu, mkuru, kapena wolamulira, wafunsira cinthu cotere kwa mlembi, kapena wopenduza, kapena Akasidi ali onse.

11 Pakuti cinthu acifuna mfumu ncapatali; ndipo palibe wina wokhoza kuciulula pamaso pa mfumu, koma milungu imene kwao sikuli pamodzi ndi anthu.

12 Cifukwa cace mfumu inakwiya, nizaza kwambiri, nilamulira kuti awaphe anzeru onse m'Babulo.

13 M'mwemo cilamuliroco cidamveka, ndi eni nzeru adati aphedwe; anafuna-funanso Danieli ndi anzace aphedwe.

(…)

17Pamenepo Danieli anapita ku nyumba kwace, nadziwitsa anzace Hananiya, Misaeli, ndi Azariya, cinthuci;

18kuti apemphe zacifundo kwa Mulungu wa Kumwamba pa cinsinsi ici; kuti Danieli ndi anzace asaonongeke pamodzi ndi eni nzeru ena a ku Babulo.

19Pamenepo cinsinsico cinabvumbulutsidwa kwa Danieli m'masomphenya a usiku. Ndipo Danieli analemekeza Mulungu wa Kumwamba.

(…)

25 Pamenepo Arioki analowa naye Danieli kwa mfumu mofulumira; natero nayo, Ndapeza munthu wa ana a ndende a Yuda, ndiye adzadziwitsa mfumu kumasulira kuja.

26 Mfumu inayankha, niti kwa Danieli, amene dzina lace ndiye Belitsazara, Ukhoza kodi kundidziwitsa lotolo ndidalilota, ndi kumasulira kwace?

27 Nayankha Danieli pamaso pa mfumu, nati, Cinsinsi inacitira liuma mfumu, angakhale anzeru, openduza, alembi, kapena alauli, sakhoza kuciululira mfumu;

28 koma kuli Mulungu Kumwamba wakubvumbulutsa zinsinsi; Iye ndiye wadziwitsa mfumu Nebukadinezara cimene cidzacitika masiku otsiriza. Loto lanu, ndi masomphenya a m'mtima mwanu pakama panu, ndi awa:

29 Inu mfumu, maganizo anu analowa m'mtima mwanu muli pakama panu, akunena za ico cidzacitika m'tsogolomo; ndipo Iye amene abvumbulutsa zinsinsi wakudziwitsani codzacitikaco.

(…)

47 Mfumu inamyankha Danieli, niti, Zoona Mulungu wako ndiye Mulungu wa milungu, ndi Mbuye wa mafumu, ndi wobvumbulutsa zinsinsi; popeza wakhoza kubvumbulutsa cinsinsi ici.

48 Pamenepo mfumu inasandutsa Danieli wamkuru, nimpatsa mphatso zazikuru zambiri, namlamuliritsa dera lonse la ku Babulo; nakhala iye kazembe wamkuru wa anzeru onse a ku Babulo.

**Mafunso**

1. Mfumu Nebukadinezara analota loto lompatsa mantha koma anaiiwala. Kodi anafunsa ciani akapolo ake? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi akapolo anayankha bwanji kulingana ndime ya 10 ndi 11?
3. Ndi cifukwa ciani Danieli ndi anzake anayenera kuphedwa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Danieli anacita ciani kulingana ndime ya 17?

5. Kodi Danieli anayankha ciani pamene mfumu anamfunsa ngati akhoza kumasulira loto lace? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Loto la mfumu lipezeka m'ndime 30-45. Litanthauza kuti kudzabwera mafumu ena amene ali ndi mphamvu pang'ono. Koma kenaka kudzabwera Yesu, mfumu wa mafumu. Cifukwa ciani timanena kuti Yesu ndi Mfumu ya mafumu onse?
7. Mfumu Yesu afuna kutilamulira. Kodi ndinu kapolo wace? Citanthauza ciani kukhala kapolo wa Yesu?

**Sewero.**
Lembani mau pa malo ao kuti mupeze yankho (Danieli 2.23).

| 14 | 4 | 9 | 11 | 21 | 25 | 1 | 13 | 9 | 11 | 1 | 14 | 9 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 |
|---|---|---|
| | | |

| 11 | 21 | 12 | 5 | 13 | 5 | 11 | 5 | 26 | 1 | 14 | 9 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | |

| 9 | 14 | 21 |
|---|---|---|
| | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **N** | **O** | **P** | **Q** | **R** | **S** | **T** | **U** | **V** | **W** | **X** | **Y** | **Z** |

## 3. Anzace a Danieli aponyedwa m’ng’anjo yamoto

**Danieli 3**
1 Mfumu Nebukadinezara anapanga fano lagolidi, msinkhu wace mikono makumi asanu ndi limodzi, ndi thunthu lace mikono isanu ndi umodzi; analiimika pa cidikha ca Dura, m'dera la ku Babulo.
2 Ndipo mfumu Nebukadinezara inatumiza kukasonkhanitsa akalonga, akazembe, ndi ziwanga, oweruza, akulu osunga cuma, mandoda, ankhoswe, ndi olamulira onse a madera, abwere kuzurula fanoli adaliimika mfumu Nebukadinezara.
(…)
7 Potero nthawi yomweyo pakumva anthu onse mau a lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ndi zoyimbitsa ziri zonse, anthu onse, mitundu ya anthu a manenedwe osiyana, anagwadira, nalambira fano lagolidi adaliimika mfumu Nebukadinezara.
8 Cifukwa cace anayandikira Akasidi ena nthawi yomweyi, naneneza Ayuda.
9 Anayankha, nati kwa mfumu Nebukadinezara, Mfumu, mukhale ndi moyo cikhalire.
10 Inu mfumu mwalamulira kuti munthu ali yense amene adzamva mau a lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ngoli, ndi zoyimbitsa ziri zonse, agwadire, nalambire fanolo lagolidi;
11 ndi yense wosagwadira ndi kulambiraadzaponyedwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto.
12 Alipo Ayuda amene munawaika ayang'anire nchito ya dera la ku Babulo, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, amuna awa, mfumu, sanasamalira inu, satumikira milungu yanu, kapena kulambira fano lagolidi mudaliimikalo.
13 Pamenepo Nebukadinezara, mumkwiyo ndi m'ukali wace, anawauza abwere nao Sadrake, Mesake, ndi Abedinego. Ndipo anabwera nao amunawa kwa mfumu.
14 Nebukadinezara anayankha, nati kwa iwo, Kodi mutero dala, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, kusatumikira milungu yanga, ndi kusalambira fano lagolidi ndinaliimikalo?
15 Mukabvomereza tsono, pakumva mau a lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ndi ngoli, ndi zoyimbitsa ziri zonse, kugwadira ndi kulambira fano ndinalipanga, cabwino; koma mukapanda kulambira, mudzaponyedwa nthawi yomweyi m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto; ndipo mulungu amene adzakulanditsani m'manja mwanga ndani?
16 Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anayankha, nati kwa mfumu Nebukadinezara, Sikufunika kuti tikuyankheni pa mlandu uwu.
17 Taonani, Mulungu wathu amene timtumikira akhoza kutilanditsa m'ng'anjo yotentha yamoto, nadzatilanditsa m'dzanja lanu, mfumu.
18 Koma akapanda kutero, dziwani, mfumu, kuti sitidzatumikira milungu yanu, kapena kulambira fano lagolidi mudaliimikalo.
19 Pamenepo Nebukadinezara anadzazidwa ndi ukali, ndi maonekedwe a nkhope yace anasandulikira Sadrake, Mesake, ndi Abedinego; anayankha, nati asonkheze ng'anjo kasanu ndi kawiri koposa umo amasonkhezera.
20 Nauza amuna ena amphamvu a m'khamu lace la nkhondo amange Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, ndi kuwaponya m'ng'anjo yotentha yamoto.
21 Pamenepo amuna awa anamangidwa ali cibvalire zopfunda zao, maraya ao, ndi nduwira zao, ndi zobvala zao zina; naponyedwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto.
22 Motero, popeza mau a mfumu anafulumiza, ndi ng'anjo inatentha koposa, lawi la moto linapha iwo aja ananyamula Sadrake, Mesake, ndi Abedinego.
23 Ndipo amuna atatu awa, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anagwa pansi omangidwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto.
24 Pamenepo mfumu Nebukadinezara anadabwa, nauka msanga, nanena nati kwa mandoda ace, Kodi sitinaponya amuna atatu omangidwa m'kati mwa moto? Anayankha nati kwa mfumu, Inde mfumu.
25 Anayankha, nati, Taonani, ndirikuona amuna anai omasuka, alikuyenda m'kati mwa moto; ndipo alibe kuphwetekwa, ndi maonekedwe a wacinai akunga mwana wa milungu.

26 Pamenepo Nebukadinezara anayandikira pa khomo la ng'anjo yotentha yamoto, analankhula, nati, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, inu atumiki a Mulungu Wam'mwambamwamba, turukani, idzani kuno. Pamenepo Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anaturuka m'kati mwa moto.
27 Ndipo akalonga, akazembe, ndi ziwanga, ndi mandoda a mfumu, atasonkhana, anaona amuna awa, kuti moto unalibe mphamvu pa matupi ao, losawauka tsitsi la pamutu pao, ndi zopfunda zao zosasandulika, pfungo lomwe lamoto losawaomba.
28 Nebukadinezara ananena, nati, Alemekezedwe Mulungu wa Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, amene anatuma mthenga wace, napulumutsa atumiki ace omkhulupirira Iye, nasanduliza mau a ine mfumu, napereka matupi ao kuti asatumikire kapena kulambira mulungu wina yense, koma Mulungu wao wao.
29 Cifukwa cace ndilamulira kuti anthu ali onse, mtundu uli wonse, ndi a manenedwe ali onse, akunenera molakwira Mulungu wa Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, adzadulidwa nthuli nthuli, ndi nyumba zao zidzasanduka dzala; popeza palibe mulungu wina akhoza kulanditsa motero.
30 Pamenepo mfumu inakuza Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, m'dera la ku Babulo.

**Mafunso**

1. Kodi mfumu anapanga ciani? M’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi akasidi anati ciani kwa mfumu zokhudza Sadrake, Mesake ndi Abedinego?
3. Mfumu anawapatsa anyamata atatu aja mpata wina kuti agwadire, koma anyamata anakana. Cifukwa ciani anakana? M’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mfumu anacita ciani pamene Sadrake, Mesake ndi Abedinego anakana kumumvera? M’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi munali amuna angati m’ng’anjo yotentha ya moto? M’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi munthu wacinayi anaoneka bwanji? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Sadrake, Mesake ndi Abedinego anaphwetekwa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
8. Mfumu anadabwa. Kodi iye anati ciani pamene Sadrake, Mesake ndi Abedinego anatuluka m’ng’anjo yotentha ya moto?
9. Abwenzi awa anamkonda Mulungu kwambiri kotero kuti sanafune kucimwa. Kodi mumacita ciani pamene munthu wina afuna inu kucita cosayenera?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho (Salimo 95.3).

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 16 | 1 | 11 | 21 | 21 | 9 |
| | | | | | |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 25 | 5 | 8 | 15 | 22 | 1 |
| | | | | | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 | 25 | 5 |
| | | | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 13 | 21 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
| | | | | | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 23 | 1 | 13 | 11 | 21 | 18 | 21 |
| | | | | | | |

| | | |
|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 |
| | | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 13 | 6 | 21 | 13 | 21 |
| | | | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 25 | 1 | 9 | 11 | 21 | 18 | 21 |
| | | | | | | |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 25 | 15 | 16 | 15 | 19 | 1 |
| | | | | | |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 13 | 9 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
| | | | | | | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 25 | 15 | 14 | 19 | 5 |
| | | | | |

| | |
|---|---|
| 1 a | 14 n |
| 2 b | 15 o |
| 3 c | 16 p |
| 4 d | 17 q |
| 5 e | 18 r |
| 6 f | 19 s |
| 7 g | 20 t |
| 8 h | 21 u |
| 9 i | 22 v |
| 10 j | 23 w |
| 11 k | 24 x |
| 12 l | 25 y |
| 13 m | 26 z |

**4. Loto la Nebukadinezara la mtengo waukuru**

**Danieli 4**
4 Ine Nebukadinezara ndinalimkupumula m'nyumba mwanga, ndi kukhala mwaufulu m'cinyumba canga,
5 Ndinaona loto lakundiopsa, ndi zolingilira za pakama panga, ndi masomphenya a m'mtima mwanga, zinandibvuta ine.
(…)
10 Masomphenya a m'mtima mwanga pakama panga ndi awa: Ndinapenya ndi kuona mtengo pakati pa dziko lapansi, msinkhu wace ndi waukuru.
11 Mtengowo unakula, nulimba, ndi msinkhu wace unafikira kumwamba, nuonekera mpaka cilekezero ca dziko lonse lapansi.
12 Masamba ace anali okoma, ndi zipatso zace zinacuruka, ndi m'menemo munali zakudya zofikira onse, nyama za kuthengo zinatsata mthunzi wace, ndi mbalame za m'mlengalenga zinafatsa m'thambi zace, ndi nyama zonse zinadyako.
13 Ndinaona m'masomphenya a m'mtima mwanga pakama panga, taonani, mthenga woyera anatsika kumwamba.
14 Anapfuulitsa, natero, Likhani mtengowo, sadzani nthambi zace, yoyolani masamba ace, mwazani zipatso zace, nyama zicoke pansi pace, ndi mbalame pa nthambi zace.
15 Koma siyani citsa ndi mizu yace m'nthaka, comangidwa ndi mkombero wa citsulo ndi mkuwa, mu msipu wa kuthengo; ncokhathamira ndi mame a kumwamba, ndi gawo lace likhale pamodzi ndi nyama ziri m'macire a m'dziko.
16 Mtima wace usandulike, usakhalenso mtima wa munthu, apatsidwe mtima wonga wa nyama, nizimpitire nthawi zisanu ndi ziwiri.
17 Citsutso ici adacilamulira amithenga oyerawo, anacifunsa, nacinena, kuti amoyo adziwe kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, naupereka kwa ali yense Iye afuna, nauutsira wolubukira anthu.
18 Loto ili ndinaliona ine mfumu Nebukadinezara; ndipo iwe, Belitsazara, undifotokozere kumasulira kwace, popeza anzeru onse a m'ufumu wanga sakhoza kundidziwitsa kumasulira kwace; koma iwe ukhoza, popeza mwa iwe muli mzimu wa milungu yoyera.
19 Pamenepo Danieli, dzina lace ndiye Belitsazara anadabwa nthawi, namsautsa maganizo ace. Mfumu inayankha, niti, Belitsazara, lisakusautse lotoli, kapena kumasulira kwace. Belitsazara anayankha, nati, Mbuye wanga, lotoli likadakhala la iwo akudana nanu, ndi kumasulira kwace kwa iwo akuutsana nanu.
20 Mtengo mudauona umene unakula, nukhala wolimba, nufikira kumwamba msinkhu wace, nuonekera pa dziko lonse lapansi,
21 umene masamba ace anali okoma, ndi zipatso zace zocuruka, ndi m'menemo munali cakudya cofikira onse, umene nyama za kuthengo zinakhala pansi pace, ndi mbalame za m'mlengalenga zinapeza pokhala pao pa nthambi yace;
22 ndinu, mfumu; mwakula, mwalimba, pakuti ukulu wanu wakula, nufikira kumwamba, ndi ufumu wanu ku cilekezero ca dziko lapansi.
23 Tsono, kuti mfumu inaona mthenga woyera wotsika kumwamba, ndi kuti, Likhani mtengowo ndi kuuononga, koma siyani citsa cace ndi mizu m'nthaka, comangidwa ndi mkombero wa citsulo ndi mkuwa, mu msipu wa kuthengo, nicikhale cokhathamira ndi mame a kumwamba, ndi gawo lace likhale pamodzi ndi nyama za kuthengo, mpaka zitampitira nthawi zisanu ndi ziwiri;
24 kumasulira kwace ndi uku, mfumu; ndipo cilamuliro ca Wam'mwambamwamba cadzera mbuye wanga mfumu:
25 kuti adzakuingitsani kukucotsani kwa anthu, ndi pokhala panu padzakhala pamodzi ndi nyama za kuthengo; ndipo mudzadya udzu ngati ng'ombe, nimudzakhala wokhathamira ndi mame a kumwamba, nizidzakupitirani nthawi zisanu ndi ziwiri, mpaka mudzadziwa kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, naupereka kwa ali yense Iye afuna mwini.
26 Ndipo kuti anauza asiye citsa ndi mizu ya mtengo, ufumu wanu udzakhazikikira inu, mukakatha kudziwa kuti Kumwamba kumalamulira.
27 Cifukwa cace, mfumu, kupangira kwanga kukomere inu, dulani macimo anu ndi kucita cilungamo, ndi mphulupulu zanu mwa kucitira aumphawi cifundo; kuti kapena nthawi ya mtendere wanu italike.
28 Conseci cinagwera mfumu Nebukadinezara.
(…)
34 Atatha masiku awa tsono, ine Nebukadinezara ndinakweza maso anga kumwamba, ndi nzeru zanga zinandibwerera; ndipo ndinalemekeza Wam'mwambamwamba, ndi kumyamika ndi kumcitira ulemu Iye wokhala cikhalire; pakuti kulamulira kwace ndiko kulamulira kosatha, ndi ufumu wace ku mibadwo mibadwo;

37 Tsono ine Nebukadinezara ndiyamika, ndi kukuza, ndi kulemekeza Mfumu ya Kumwamba, pakuti nchito zace zonse nzoona, ndi njira zace ciweruzo; ndi oyenda m'kudzikuza kwao, Iye akhoza kuwacepetsa.

**Mafunso**

1. Chulani dzina la munthu amene analota loto kulingana ndi Danieli 4 ndime ya 4.
2. M’loto lake mfumu Nebukadinezara anaona mngelo. Kodi mngelo ananena ciani? M’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi ndani amene anamasulira loto? M’ndime iti mwapeza yankho?
4. Mfumu Nebukadinezara inali yamphamvu (monga mtengo wamphamvu). Koma sinabvomereza kuti Mulungu ndi Wamphamvuyonse wompatsa mphamvu ndi nzeru. Kodi Danieli anapangira ciani mfumu kulingana ndi ndime ya 27?
5. Nanga inu ndinu munthu wodzikweza? Kodi kutsutsidwa ndi kwabwino?
6. Kodi mfumu Nebukadinezara inabvomereza ciani itaciritsidwa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi mumavomereza kuti Mulungu ndi Mfumu imene imalamulira zonse? Ngati inde, mumacitapo ciani? Ngati iai, ganiziranipo za upangiri wa Danieli.

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

| 16 | 1 | 11 | 21 | 20 | 9 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 13 | 21 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 | 25 | 5 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 23 | 15 | 23 | 5 | 18 | 21 | 26 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | |

| 1 | 3 | 8 | 5 | 16 | 19 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 23 | 9 | 21 | 1 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 14 | 1 | 11 | 21 | 26 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 23 | 9 | 14 | 1 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 | 14 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M | N |

| 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## 5. Madyerero a Belisazara, dzanja lolemba pakhoma

**Danieli 5**

1 Mfumu Belisazara anakonzera anthu ace akulu cikwi cimodzi madyerero akuru, namwa vinyo pamaso pa cikwico.

2 Belisazara, pakulawa vinyo, anati abwere nazo zotengera za golidi ndi siliva adazicotsa Nebukadinezara atate wace ku Kacisi ali ku Yerusalemu, kuti mfumu ndi akuru ace, akazi ace ndi akazi ace ang'ono, amweremo.

3 Nabwera nazo zotengera zagolidi adazicotsa ku Kacisi wa nyumba ya Mulungu ya ku Yerusalemu, ndipo mfumu ndi akuru ace, akazi ace ndi akazi ace ang'ono, anamweramo.

4 Anamwa vinyo, nalemekeza milungu yagolidi, ndi yasiliva, yamkuwa, yacitsulo, yamtengo, ndi yamwala.

5 Nthawi yomweyo zinabuka zala za dzanja la munthu, nizinalemba pandunji pa coikapo nyali, pomata pa khoma la cinyumba ca mfumu; ndipo mfumu inaona nsonga yace ya dzanja lidalembalo.

6 Pamenepo padasandulika pa nkhope pace pa mfumu, ndi maganizo ace anamsautsa, ndi mfundo za m'cuuno mwace zinaguruka, ndi maondo ace anaombana.

7 Nipfuulitsa mfumu abwere nao openda, Akasidi, ndi alauli, Mfumu inalankhula, niti kwa anzeru a ku Babulo, Ali yense amene adzawerenga lemba ili, nadzandifotokozera kumasulira kwace, adzabvekedwa cibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi mwace, nadzakhala wolamulira wacitatu m'ufumuwu.

8 Pamenepo analowa anzeru onse a mfumu, koma sanakhoza kuwerenga lembalo, kapena kudziwitsa mfumu kumasulira kwace.

13 Pamenepo analowa naye Danieli kwa mfumu. Mfumu inayankha, niti kwa Danieli, Ndiwe kodi Danieli uja wa ana a ndende a Yuda, amene mfumu atate wanga anatenga ku Yuda?

14 Ndamva za iwe kuti muli mzimu wa milungu mwa iwe, ndi kuti mupezeka mwa iwe kuunika, ndi luntha, ndi nzeru zopambana.

15 Ndipo tsono anabwera nao kwa ine anzeru, openda, kuti awerenge lemba ilo, ndi kundidziwitsa kumasulira kwace; koma sanakhoza kufotokozera kumasulira kwa cinthuci.

16 Koma ndamva ine za iwe, kuti ukhoza kutanthauzira mau, ndi kumasula mfundo; tsono ukakhoza kuwerenga lembalo, ndi kundidziwitsa kumasulira kwace, udzabvekedwa cibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi mwako; nudzakhala wolamulira wacitatu m'ufumuwo.

17 Pamenepo anayankha Danieli, nati kwa mfumu, Mphatso zanu zikhale zanu, ndi mphotho zanu mupatse wina; koma ndidzawerengera mfumu lembalo, ndi kumdziwitsa kumasulira kwace.

18 Mfumu inu, Mulungu Wam'mwambamwamba anapatsa Nebukadinezara atate wanu ufumuwu, ndi ukulu, ndi ulemerero, ndi cifumu;

19 ndipo cifukwa ca ukulu adampatsawo anthu onse, mitundu yonse ya anthu, a manenedwe onse, ananjenjemera, naopa pamaso pace; amene anafuna kuwapha anawapha; amene anafuna kuwasunga anawasunga amoyo; amene anafuna kuwakweza anawakweza; amene anafuna kuwatsitsa anawatsitsa.

20 Koma pokwezeka mtima wace, nulimba mzimu wace kucita modzikuza, anamtsitsa pa mpando wa ufumu wace, namcotsera ulemerero wace;

21 ndipo anamuinga kumcotsa kwa ana a anthu, ndi mtima wace unasandulika ngati wa nyama za kuthengo, ndi pokhala pace mpa mbidzi, anamdyetsa udzu ngati ng'ombe, ndi thupi lace linakhathamira ndi mame a kumwamba; mpaka anadziwa kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, nauikira ali yense Iye afuna mwini.

22 Ndipo inu mwana wace, Belisazara inu, simunadzicepetsa m'mtima mwanu, cinkana munazidziwa izi zonse;

23 koma munadzikweza kutsutsana naye Ambuye wa Kumwamba; ndipo anabwera nazo zotengera za nyumba yace kwa inu; ndi inu ndi akuru anu, akazi anu ndi akazi anu ang'ono, mwamweramo vinyo; mwalemekezanso milungu yasiliva, ndi yagolidi, yamkuwa, yacitsulo, yamtengo, ndi yamwala, imene siiona,

kapena kumva, kapena kudziwa; ndi Mulungu amene m'dzanja mwace muli mpweya wanu, ndi njira zanu zonse, yemweyo simunamcitira ulemu.
24 Pamenepo nsonga ya dzanja inatumidwa kucokera pamaso pace, nililembedwa lembali.
25 Ndipo lemba lolembedwa ndi ili: MENE MENE TEKEL UF ARSIN.
26 Kumasulira kwace kwa mau awa ndi uku: MENE, Mulungu anawerenga ufumu wanu, nautha.
27 TEKEL, Mwayesedwa pamiyeso, nimupezeka mwaperewera.
28 PERES, ufumu wanu wagawika, nuperekedwa kwa Amedi ndi Aperisi.
29 Pamenepo Belisazara analamulira, ndipo anabveka Danieli cibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi mwace, nalalikira za iye kuti ndiye wolamulira wacitatu m'ufumumo.
30 Usiku womwewo Belisazara mfumu ya Akasidi anaphedwa.

**Mafunso**

1. Belisazara anakonzera anthu madyerero akulu. Kodi mfumu analamulira ciani kuti zibweretsedwe kumadyerero? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi ndi ciani cinacitika ku madyerero kulingana ndi ndime ya 5?
3. Kodi anzeru onse anatha kumasulira mau olembedwa pa cipupa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Danieli anakhoza kumasulira mau olembedwa pa cipupa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Werengani ndime 27 ndi 28. Kodi mau olembedwa pa cipupa anatanthauza ciani?
6. Ndi ciani cinacitika ndi mfumu usiku womwewo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Ifenso tiyenera kufa cifukwa ca macimo athu. Kodi njira ya kupulumutsidwa kwa macimo ndiyo ciani?

**Sewero**

Pezani mau onse ndipo lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| m | u | l | m | u | l | u | n | g | u |
| m | a | d | y | e | r | e | r | o | u |
| m | m | t | i | m | a | i | u | m | n |
| u | g | m | u | n | l | m | u | v | d |
| n | i | a | y | e | e | f | w | i | d |
| t | o | u | l | w | y | a | e | n | z |
| h | r | n | k | h | o | p | e | y | a |
| u | a | m | p | h | o | t | h | o | n |
| d | u | z | m | z | i | m | u | a | j |
| b | e | l | i | s | a | z | a | r | a |

| | | | |
|---|---|---|---|
| dzanja | Danieli | Mulungu | Belisazara |
| madyerero | munthu | nkhope | vinyo |
| imfa | ufumu | mphotho | mzimu |
| mtima | | | |

Yankho: ……………………………………………………………………………………………………………….(Salimo 75.7)

## 6. Akalonga amchulira Danieli cifukwa kwa Dariyo

**Danieli 6**

1. Kudamkomera Dariyo kuikira ufumuwo akalonga zana limodzi mphambu makumi awiri akhale m'madera onse a ufumu;
2. Ndi akuyang'anira iwo akulu atatu, woyamba wao ndi Danieli; kuti akalonga awa adziwerengere kwa iwo, ndi kuti za mfumu zisasoweke.
3. Pamenepo Danieli amene anaposa akuluwa ndi akalonga, popeza munali mzimu wopambana mwa iye, ndi mfumu inati imuike woyang'anira ufumu wonse.
4. Ndipo akuluwa ndi akalonga anayesa kumtola cifukwa Danieli, kunena za ufumuwo koma sanakhoza kupeza cifukwa kapena colakwira, popeza anali wokhulupirika ndipo sanaona cosasamala kapena colakwa ciri conse mwa iye.
5. Pamenepo anthu awa anati, sitidzamtola cifukwa ciri conse Danieli amene, tikapanda kumtola ici pa cilamulo ca Mulungu wace.
6. Ndipo akuru awa ndi akalonga anasonkhana kwa mfumu mofulumira, natero nayo, Mfumu Dariyo, mukhale ndi moyo cikhalire.
7. Akuru onse a ufumuwo, ndi akazembe ndi akalonga, mandoda, ndi ziwanga, anapangana kukhazika lemba lacifumu, ndi kuikapo coletsa colimba, kuti ali yense akapempha kanthu kwa mulungu ali yense, kapena kwa munthu ali yense masiku makumi atatu, osati kwa inu nokha, mfumu, adzaponyedwa m'dzenje la mikango.
8. Tsopano, mfumu, mukhazikitse coletsaco, ndi kutsimikiza colembedwaco, kuti cisasinthike monga mwa malamulo a Amedi ndi Aperisi, amene sasinthika.
9. Momwemo mfumu Dariyo anatsimikiza colembedwa ndi coletsaco.
10. Ndipo podziwa Davide kuti adatsimikiza colembedwaco, analowa m'nyumba mwace, m'cipinda mwace, cimene mazenera ace anatseguka oloza ku Yerusalemu; ndipo anagwada maondo ace tsiku limodzi katatu, napemphera, nabvomereza pamaso pa Mulungu wace monga umo amacitira kale lonse.
11. Pamenepo anasonkhana anthu awa, napeza Danieli alikumpemphera ndi kupembedza pamaso pa Mulungu wace.
12. Ndipo anayandikira, nanena pamaso pa mfumu za coletsaco ca mfumu, Kodi simunatsimikiza coletsaco, kuti ali yense akapempha kanthu kwa mulungu ali yense, kapena kwa munthu ali yense, masiku makumi atatu, osati kwa inu nokha, mfumu, adzaponyedwa m'dzenje la mikango? Mfumu niyankha, niti, Coona cinthuci, monga mwa malamulo a Amedi ndi Aperisi amene sasinthika.
13. Pamenepo anayankha, nati pamaso pa mfumu, Danieli uja wa ana a ndende a Yuda sasamalira inu, mfumu, kapena coletsa munacitsimikizaco; koma apempha pemphero lace katatu tsiku limodzi.
14. Ndipo mfumu m'mene atamva mau awa anaipidwa kwambiri, naika mtima wace pa Danieli kuti amlanditse, nayesetsa mpaka polowa dzuwa kumlanditsa.
15. Koma anthu awa anasonkhana kwa mfumu, nati kwa mfumu, dziwani, mfumu, kuti lamulo la Amedi ndi Aperisi, ndilo kuti coletsa ciri conse ndi lemba liri lonse idazikhazikira mfumu, zisasinthike.
16. Pamenepo inalamula mfumu, ndipo anadza naye Danieli, namponya m'dzenje la mikango. Ndipo mfumu inalankhula, niti kwa Danieli, Mulungu wako amene umtumikira kosalekeza, Iyeyu adzakulanditsa.
17. Ndipo anatenga mwala, nauika pakamwa pa dzenje, niukomera mfumu ndi cosindikizira cace, ndi cosindikizira ca akuru ace, kuti kasasinthike kanthu ka Danieli.
18. Pamenepo mfumu inamuka ku cinyumba cace, nicedzera kusala usikuwo, ngakhale zoyimbitsa sanabwera nazo pamaso pace, ndi m'maso mwace munamuumira.
19. Nilawira mamawa mfumu, nimuka mofulumira ku dzenje la mikango.
20. Ndipo poyandikira padzenje inapfuula ndi mau acisoni mfumu, ninena, niti kwa Danieli, Danieli, mnyamata wa Mulungu wamoyo, kodi Mulungu wako, amene umtumikira kosalekeza, wakhoza kukulanditsa kwa mikango?
21. Pamenepo Danieli anati kwa mfumu, Mfumu, mukhale ndi moyo cikhalire.

22. Mulungu wanga watuma mthenga wace, natseka pakamwa pa mikango; ndipo siinandipweteka, cifukwa anandiona wosacimwa pamaso pace, pamaso panunso, mfumu, sindinalakwa.
23. Pamenepo mfumu inakondwera kwambiri, niwauza aturutse Danieli m'dzenje. Momwemo anamturutsa Danieli m'dzenje, ndi pathupi pace sipadaoneka bala, popeza anakhulupirira Mulungu wace.
24. Ndipo italamulira mfumu, anabwera nao amuna aja adamneneza Danieli, nawaponya m'dzenje la mikango inawaposa mphamvu, niphwanya mafupa ao onse.

**Mafunso**

1. Fotokozani mwa chidule zimene zinachitika m' nkhani imeneyi.
2. Cifukwa ciani Danieli anaponyedwa mu dzenje la mikango? M'ndime iti mwapeza yankho?
3. Nanga inu, mumacita ciani pamene anthu afuna kuti muleka kupembedza Mulungu?
4. Kodi cinacitika ciani mu dzenje la mikango? M'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi cinacitika ndi ciani tsiku la mawa? M'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi cinacitika ciani ndi anthu amene anauza mfumu kupanga lamulo la tsopano? M'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi tingaphunzire ciani pa nkhani iyi?

**Sewero**


Lembani mau awa pa malo ao.

- babulo
- mikango
- moto
- danieli
- hananiya
- mfumu
- pemphero
- imfa
- yotentha
- dzanja
- nzeru
- misaeli
- nyengo
- madyerero
- azariya
- loto
- kumwamba
- mphamvu
- mtengo
- mau
- munthu
- ndipo
- cipupa
- cakudya
- atumiki
- atatu
- msipu
- openda

Lembani yankho:

……………………………………………………………………………………………………………………………………………………………

……………………………………………………………………………………………………………………………………………………(Salimo 46.1)


O
B
L
Y
H
T
K
D
Y
F
N
S
P
M
T
V
A
W
M
Z
U
P
D
D
J
T
H
F